# ZIFUKWA ZINAYI ZOKUPANGISANI KUMWETULIRA



## Kumwetulira koyamba

## Mulungu amakukondani kwambiri

**Pakuti Mulungu anakonda dziko lapasi kotero anapereka mwana wake obadwa yekha kuti yense okhulupirira iye asatayike koma akhale nawo moyo wosatha** (Yohane 3 v 16)

Posatengera mmene mukumvera kapena zomwe mwadutsamo, mphamvu yachikondi cha Mulungu pa inu siyisintha. Iye anapereka mwana wake mmalo mwanu.

## Kumwetulira kwachiwiri

## Yesu anakuferani

Chizindikiro chachikondi chenicheni ndi pamene munthu walolera kufa mmalo mwa mnzake. Kulibeso chikondi chachikulu ngati ichi. Mbiri imatiuza kuti Yesu anakhala ndi moyo, nafa imfa yapamtanda. Baibulo limati izi anachita chifukwa cha inu ndi ine.

**Pakuti onse anachimwa naperewera paulemerero wa Mulungu** (Aroma 3 v 23)

**Pakuti mphoto yauchimo ndi imfa koma mphatso yaulele ya Mulungu ndi moyo wosatha mwa Yesu Khristu** (Aroma 6 v 23)

**Koma Mulungu anaonetsa chikondi chake kwa ife mwa ichi; kuti pamene tinali ochimwa, Khristu anatifera ife** (Aroma 5 v 8)

**Iye anaperekedwa ndi kukaphedwa chifukwa cha machimo athu, ndipo anauka kwa akufa kutiyanjanitsa ndi Mulungu** (Aroma 4 v 25)

## Kumwetulira kwachitatu

### Mulungu ali ndi cholinga ndi moyo wanu

**Pakuti ndidziwa malingaliro amene ndilingirira inu, ati Yehova, malingariro a mtendere, si a choipa ayi; akukupatsani inu tsogolo ndi chiyembekezo** (Yeremiya 29 v 11)

Kuseri kwa cholengedwa chilichose kuli olenga. Mkati mwa cholengedwa chilichose muli cholinga cha amene analengayo. Inu ndi opatulika kwa Mulungu ndipo ali ndi cholinga ndi moyo wanu. Cholinga choyamba cha Mulungu ndikuti mudziwe chikondi chake pa inu, ndipo chilichose chizakhala mmalo mwake pamene inu mwakhulupirira chikondi chake.

## Kumwetulira kwachinayi

### Lero ndi tsiku lanu

**Taonani lero ndi tsiku lako lachipulumutso** (2 Akorinto 6 v 2)

**Yesu, ameneyu Mulungu anamuukitsa kwa akufa tsiku lachitatu, namuonetsera poyera** (Machitidwe 10 V 40)

**Ngati udzavomereza ndipakamwa pako kuti Yesu ndi Ambuye, ndikukhulupirira mumtima mwako kuti Mulungu anamuwukitsa kwa akufa, udzapulumuka** (Aroma 10 v 9)

Mpweya omwe mumapuma ndi mphatso yochokera kwa Mulungu. Iye anakulengani m'chifaniziro chake ndipo amakukondani kwambiri. Kumbukirani mulibe lonjezano lamawa koma muli ndi danga lalero, tsopano, kuti mulape ndikulandira mphatso ya Mulungu mwa Yesu Khristu. Mtanda wa Yesu Khristu sichinali chilengezo cha chifooko kapena ndale zachipembedzo, koma inali mphamvu yotiyeretsa kuchoka ku uchimo kutibweretsera mtendere pakati pa ife ndi Mulungu. Musafe opanda Khristu.

# Musachedwenso ayi; pempherani pemphero ili ndi ine

Mulungu wanga wakumwamba, mu dzina la Yesu, ndikhululukireni machimo anga. Ndikukhulupirira kuti Yesu ndi mwana wa Mulungu amene anakhala ndi moyo, nafa ndipo munamuukitsa chifukwa cha chikondi chanu pa ine. Ambuye Yesu lowani mumtima mwanga ndipo mukhale Ambuye wa moyo wanga. Ndipatseni tsopano chitsimikizo cha chipulumutso changa chimene ndi Mzimu Woyera, ndikuti andidzadze mumtima mwanga poti ndine mwana wanu. Mudzina la Yesu ndapemphera. Amen.

## Pemphero langa kwa inu

Atate Mulungu wanga, mu dzina la Yesu ndikumasula kudzoza kwanu kwa Mzimu Woyera kuti kuphimbe ndi kuphwanya goli lililonse la kusakhulupirira ndi kusokonezeka pa munthu uyu. Ndikulengeza kuti angelo otumikira amuzungulire ndi kumuteteza ndikumuthandiza. Atate, pitirizani kuvumbulutsa choonadi chanu ndi chikondi chanu kwa munthu wamtengo wake uyu. Chilitsani thupi lake ndi kumasula malingaliro ake mu dzina la Yesu. Amen.

Ndikukuitanirani Ku tsamba ili

**www.foursmiles.com**

©2019 FourSmiles Productions. Used by permission.